

Banja laling'ono, umoyo wathanzi mboma la Balaka

Banja la anthu ochepa limapindula mokwanila kuchokela ku zithandizo zosiyanasiyana za mdziko zokhudza miyoyo yawo.

- Mu zaka makumi awiri zapitazi chiwerengero cha anthu mu mzinda wa Balaka chachulukitsidwa ka ½ kuchoka pa anthu 97 kufika pa anthu 145 pa km² ili yonse.
- Nyumba zokhala anthu zisanu ndi ziwiri (7) mwa nyumba zisanu ndi zitatatu (8) zili zones zili ndi potunga madzi a ukhondo pa makono.



Nyumba zokhala anthu zisanu ndi zinayi (9) mwa nyumba khumi (10) zili zonse zimagwilitsa ntchito nkhuhi pophika; ndipo nyumba imodzi (1) yokha mwa nyumba makumi awiri (20) zili ndi magetsi.


Amayi amodzi (1) okha mwa amayi khumi ndi mmodzi (16) aliwonse; komanso abambo amodzi (1) mwa azibambo khumi ndi amodzi (11) aliwonse ndi amene amamaliza maphunziro awo a ku sekondale.

- Amayi atatu (3) mwa amayi anayi (4) aliwonse komanso abambo anayi (4) mwa abambo asanu (5) aliwonse amadziwa kulemba, kuwelenga ndi kuwelengera.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi atatu (8) aliwonse komanso abambo amodzi (1) mwa abambo asanu ndi atatu (8) aliwonse sali pa ntchito iliyonse yolembedwa.
- Amayi anayi (4) mwa amayi asanu ndi awiri (7) aliwonse amavutika kwambiri kupeza chithandizo cha mankhwala akad wala chifukwa zipatala zoyandikila ndi kumene amakhala zili kutali kwambiri.

Ubwino wotsatira njira za kulera

Banja likakhala ndi ana ochepa, zimathandiza makolo a anawa kuwaphunzitsa mokwanila ana awo ndipo chifukwa choti aphunzira bwino, anawa amakhala ndi mwayi wozeza ntchito zabwino mtsogolo. Kuchepetsa kachulukidwe ka anthu mdziko kumathandiza boma ndi mabungwe othandiza boma kukonzekera bwino pa ntchito zopititsa umoyo wa anthu patsogolo monga kukhala ndi madzi a ukhondo, ntchito za umoyo komanso za mtengatenga.

Anthu awiri mwa anthu atatu aliwonse mbomali ali ndi zaka zosapitilira makumi awiri ndi zisanu (25)



Source: National Statistical Office of Malawi, Population Projections Malawi.

Banja la anthu ochepa limakhala ndi mayi wa moyo wathanzi komanso banjalo limakhala losangalala



Amayi amabeleka ana asanu ndi mmodzi (6) pa moyo wao wonse koma amaonetsa chidwi chobeleka ana anayi (4) wokha pa moyo wao wonse.

Amayi amodzi (1) mwa amayi atatu (3) aliwonse a zaka za pakati pa khumi ndi zisanu (15) ndi zaka khumi ndi zisanu ndi zinayi (19) ayamba kale kubeleka ana.

- Amayi awiri (2) mwa amayi asanu ndi awiri (7) aliwonse amabelekela kunyumba osati kuchipatala.
- Amayi atatu (3) mwa amayi asanu ndi awiri (7) aliwonse omwe ali pa banja amatsata njira za kulera; ndipo amayi amodzi (1) mwa amayi anayi (4) aliwonse amatsa njira zolererazi kuti asabeleke ana ambiri.
- Amayi amodzi (1) mwa amayi makumi awiri (20) aliwonse komanso abambo amodzi (1) mwa abambo makumi awiri (20) aliwonse amakhulupilira kuti ndi zovomelezeka kuti mamuna akhoza kumenya mkazi wake nthawi zina.

Ubwino wotsatira njira za kulera

Amayi amodzi (1) mwa amayi asanu ndi amodzi (6) aliwonse a zaka zapakati pa khumi ndi zisanu (15) ndi makumi anayi ndi zisanu (49) amamwalira pa nthawi yobeleka mwana. Kutsatila njira za kulera kumathandiza amayi omwe ndi achichepeleko kutenga nthawi asanakhale ndi mimba (pathupi) ndipo kutenga nthaw chonchi kumathandiza kuti asapeze mavuto nthupi mwawo omwe amadza chifukwa chobeleka akadali ang'ono. Amayi ngati akhala ndi ufulu wosankha nthawi yoti abeleke komanso kusiyantsa zaka za ana obelekedwa zimawathandiza kuti akhale ndi moyo wathanzi. Ana omwe amayi awo amamwalira nthawi zambiri samamaliza maphunziro awo ku sukulu.




Mdziko la Malawi, amayi amodzi amamwalira pobeleka ana pa ma ola awiri aliwonse.



Mwana wakhanda mmodzi (1) wosakwana chaka chimodzi amamwalira ma ola asanu ndi atatu (8) aliwonse.

Banja la anthu ochepa ana ake amakula bwino komanso amakhala ndi moyo wathanzi

- Mwana mmodzi (1) mwa ana khumi ndi anayi (14) aliwonse wochepera zaka zisanu (5) amakhala ndi thupi lopelelela losagwilizana ndi msinkhu wawo.



Ana anayi (4) mwa ana asanu ndi anayi (9) aliwonse wochepera zaka zisanu (5) amakhala wopinimbira.

Ubwino wotsatira njira za kulera

Kutsatila njira za kulera kumathandiza ma banja kuti ana awo akule ndi moyo wathanzi komanso kutha kuonetsetsa kuti pakupita nthawi yokwanila bwino pamene mwana wabadwa ndi nthawi yomwe mwana wina akudzabadwanso mbanjamo. Ana obadwa mosiyana ndi zaka zitatatu kapena kupitilira apo amakhala ndi mwayi wokhala moyo wochulukira kwambiri kuposa ana omwe abadwa mosiyana ndi zaka ziwiri kapena kuchepela apo. Makolo omwe ali ndi ana ochepa amasalira bwino ana awo ndi kuwapatsa zakudya zokwanila.



Pa ma ola asanu (5) aliwonse mwana mmodzi wosakwanitsa zaka zisanu amamwalira.